SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: CHIPHUNZITSO CHA YESU CHA PA PHIRI
TSIKU LOYAMBA: IFE TIMADALITSIDWA TIKAMAVUTIKA

1. Sabata yapita tinaona mmene Yesu anasankhira ndi kutsogolera ophunzira ake. Iye anali ndi zinthu zambiri zoŵaphunzitsa iwo. Nthaŵi zina kunali kovuta kwa Iye kupeza nthaŵi yoŵaphunzitsira. Anthu anali kuunjikira kulikonse komwe Yesu anali. Chifukwa cha ichi Yesu anatengera ophunzira ake kuphiri.

Kodi Yesu anali kuchita chiyani pamene ophunzira ake anachita zolakwa?

______________________________________________

Pamene Yesu amatidzudzula monga ophunzira ake, kodi Iye amafuna kuti ife tichite chiyani?

______________________________________

======================================================================

2. Ophunzira akachita zolakwa, Yesu anali kuŵadzudzula iwo. Pamene Yesu ali kutidzudzula amafuna kuti ife titembenuke kuchoka ku uchimo wathu. Tsiku lina Yesu anapita ndi ophunzira ake ku phiri. Anthu ena amaopa mapiri. Koma Yesu anapeza kuti ndi malo abwino ophunzitsirako. Sabata ino ndi sabata yamaŵa tidzaphunzira zimene Iye anaphunzitsa ophunzira ake. Phunziro lalero ndi lakuti:

(1) Kuchokera pa ulaliki wa Yesu wa pa phiri, amene amva njala yachilungamo adzakhutitsidwa.

(2) Amene ali woyera mumtima adzaona Mulungu.

(3) Amene amalondedwa chifukwa cha chilungamo adzalandira mphotho yaikulu m'mwamba.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuŵerenga, Mateyu 5:1 mpaka 12. Kodi anthu ambiri amakhala okondwa pamene ali wosauka, akulira, ndi anjala?

______________________________

======================================================================

3. Iwo asakhala okondwa. Iwo amakhala achisoni. Iwo amaganiza kuti miyoyo yawo ndi yosadalitsidwa. Koma Yesu ananena chinthu chodabwitsa. Iye anati ndi kwabwino ngati muli kuona kuti ndinu wosalemera kapena

kunyada mu mzimu. Ndi kwabwino ngati mutalirira zimenezi.

Mateyu 5:3-4:

> Odala ali osauka mu mzimu chifukwa uli wawo Ufumu wa kumwamba.
> Odala ali achisoni chifukwa adzasangalatsidwa.

M'ndime zimenezi, ngati tiri osauka mumzimu ndipo ngati titamalira za zosoŵa zathu za uzimu, kodi ndife odala kapena wotembereredwa?

______________________________

==========================================================================

4. Ndife odala. Tikhoza kukhala wokondwa. Zimenezi ndi zinthu zodabwitsa! Pamene tili kuona chosoŵa chathu, ndi kwabwino. Timadziŵa kuti timasoŵeka thandizo la Mulungu. Timadziŵa kuti Mulungu akhoza kusintha mizimu yathu yosaukayi. Iye akhoza kutonthoza kulira kwathu. Iye adzatidalitsa chifukwa tiri kuona zosoŵa zathu.

Mateyu 5:5-6:

> Odala ali akufatsa, chifukwa adzalandira dziko lapansi.
> Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta.

Ife ndife odala ngati tiri ndi njala. Kodi timayenera kukhala ndi njala ya chiyani?

______________________________

==========================================================================

5. Timayenera kukhala ndi njala ya chilungamo. Sitiyenera kukhala a njala ya ulemerero kapena chuma. Sitiyenera kukhala ndi njala ya malo ofunika kapena mphamvu zazikulu. Tiri osauka mumzimu. Zimenezi sizitanthauza kuti tiribe mzimu. Zimatanthauza kuti ife sindife onyada. Timalirira machimo athu. Ndife odzichepetsa. Yesu amati odzichepetsa ndi okondwa chifukwa iwo adzalandira dziko lapansi.

Ngati ife tiri osauka mu mzimu, kodi tidzafuna chilungamo motani?

______________________________

==========================================================================

6. Ife tidzakhala ndi njala ya chilungamo. Tidzafuna chilungamo chochulukira. Tidzidziona kuti sitinafike pokwaniritsa zonse zimene Mulungu akufunira kuti tikhalire. Tidzakhala tiri kulirira machimo athu. Tidzakhala odzichepetsa ndipo tidzakhala ndi njala ya chilungamo. Tidzafunitsitsa kukhala monga Yesu mu zonse zimene timanena ndi zimene tichita.

Mateyu 5: 6:

> Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo, chifukwa adzakhuta.

Kodi ndi madalitso otani amene Yesu anati adzabwera kwa ife ngati tiri ndi njala ya chilungamo?

______________________________

==============================

7. Ife tidzakhuta. Tidzakhala odzazidwa ndi chilungamo. Tidzakhala ndi miyoyo yabwino. Zimenezi ndi zodabwitsa! N'chifukwa chake Yesu anati ndife odala. Pamene tidziona ife eni bwino timalakalaka kukhala monga Mulungu. Timafuna kukhala miyoyo yoyera yofanana ndi moyo wa Yesu. Ife timadziŵa kuti timamusoŵa Iye.

Kuchokera pa ulaliki wa Yesu wa pa phiri, kodi ndi ndani amene adzakhuta?

______________________________

==============================

8. Amene ali ndi njala ya chilungamo adzakhuta. Iwo ndi odala. Ngati sitimaona zosoŵa zathu, Mulungu sadzatithandiza ife. Ngati tiribe njala sitingakhale okhutitsidwa. Koma ngati tiri ndi zosoŵa, tikhoza kuthandizidwa. Ngati tiri ndi njala, Mulungu amagwira ntchito mwa ife. Iye amaika chilungamo mwa ife, timakhala ndi chipatso cha moyo wa Chikhristu.

Mateyu 5:7-8:

> Odala ali akuchitira chifundo; chifukwa adzalandira chifundo.
> Odala ali oyera mtima; chifukwa adzaona Mulungu.

Ngati ife tiri oyera mumtima, kodi tidzaona ndani? ______________

==============================

9. Tidzaona Mulungu. Ife tiri odala pamene tiri olungama ndi anthu komanso olungama kwa Mulungu. Tikamakhala a chifundo ndi anthu kumasonyeza kuti tiri kuŵakonda. Timakhala bwino nawo. Ndife olungama nawo. Kukhala oyera mumtima kumaonetsa kuti tiri ndi cholungamo ndi Mulungu. Timavomereza machimo athu ndipo Iye amaŵachotsa.

Mateyu 5:8:

Odala ali oyera, chifukwa adzaona Mulungu.

Kuchokera ku mawu a Yesu ameneŵa, kodi ife timayenera kukhala otani mumtima kuti tidzaone Mulungu?

________________________________________

============================================================

10. Timayenera kukhala angwiro kapena oyera. Ife sitingathe kukhaladi okondwa ngati muli tchimo m'mitima mwathu. Anthu ena amaganiza kuti madalitso amadza ndi ndalama kapena zinthu. Iwo amaganiza kuti madalitso amabwera pokhala ndi mphamvu yoposa anthu ena. Koma Yesu asanavomerezane ndi zimenezi.

Mitima yathu iyenera kukhala yoyera. Izi ndi zovuta chifukwa sitingathe kutsuka mitima yathu. Sitingathe kupanga maganizo athu kuti akhale angwiro. Ife sitingathe kudzipanga kukhala okondwa ngati tiri m'machimo. Ndipo sindife oyenera kuona Mulungu. Koma pali wina wake amene angatisinthe ndi kupanga mitima yathu kukhala yoyera.

Kodi ndi ndani amene tsiku lina tidzakamuona ngati tiri oyera mtima?

________________________________________

============================================================

11. Tidzakaona Mulungu. Tidzakhala monga Iye. Tidzakhala oyenera kukhala ndi Iye. Tikhoza kuyamba kumuona Iye tsopano padziko lapansi lino Timakhoza kuyamba kumvetsetsa dongosolo lake pa ife. Wophunzira Yohane analemba za kalata iyi.

1 Yohane 3:2:

Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sichinaoneke chimene tidzakhala, tidziŵa kuti, pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali.

Kuchokera pa ulaliki wa Yesu wa pa phiri, kodi ndi ndani amene adzaone Mulungu?

________________________________________

Kodi ndi ndani amene adzakhuta? ______________________________

______________________________________________________________

==============================================================

12. Oyera mumtima adzaona Mulungu. Amene ali ndi njala ya chilungamo adzakhutitsidwa. Anthu amene satsata Khristu ali ndi maganizo osiyana a zakukhala odalitsidwa. Iwo amaganiza kuti tikakhala ndi moyo wopanda mavuto ndiye madalitso. Tikakhala ndi ndalama zambiri ndiye ife odalitsidwa. Koma Yesu amati ndife odalitsidwa m'njira ina.

Mateyu 5:9-10:

> Odala ali akuchita mtendere; chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu. Odala ali akunzunzidwa chifukwa cha chilungamo: chifukwa uli wao Ufumu wa kumwamba.

Kodi ife ndife odala ngati tiri kulondedwera chiyani? ______________

______________________________________________________________

==============================================================

13. Ife ndife odalitsidwa ngati tiri kulondedwera chilungamo. "Kulondedwa" ndi mawu a mphamvu. Kumatanthauza kuti kukhala ovutidwa ndi anthu ena. Kumatanthauza kukhala ovutidwa chifukwa chakuti ndife Akhristu. Ambiri a ife tiri ndi ufulu wokhala Akhristu ngati tiri kufuna kutero. Koma m'maiko ena, Akhristu amadedwa. Iwo samaloredwa kumakomana ndi Akhristu ena. Iwo samaloredwa kumayimba ndi kumapemphera. Iwo amadedwa monga zinyama. Yesu anati anthu ameneŵa ndi odala!

Mateyu 5:11-12:

> Odala muli inu mmene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa zirizonse chifukwa cha ine. Sekerani, sangalalani; chifukwa mphotho yanu ndi yaikulu m'mwamba.

Kodi tidzakalandira chiyani kumwamba ngati tiri kukhala m'moyo wolondedwalondedwa kuno?

______________________________________________________________

==============================================================

14. Tidzakalandira mphotho. Mulungu samaiŵala amene akhala ndi moyo wovutika chifukwa chokhala Akhristu. Yesu anadziŵa kuti akuphunzira adzakhala ndi nthaŵi yamavuto. Anthu ambiri adzayesa kuŵavuta ndi kuŵapha iwo. Yesu anati adzakhala ndi mavuto m'dziko. Koma iye anati iwo adzadalitsidwa.

Kodi ndi ndani ali odala chifukwa chakuti mphotho yawo ndi yaikulu m'mwamba?

________________________________________

==========================================================================

15. Ndi amene ali kulondedwa chifukwa cha chilungamo. Kapena nthaŵi zina inu mumadedwa chifukwa chakukhala Mkhristu. Anthu mwina anayesa kufuna kukuphani. Yesu anati muyenera kukhala osangalala. Khalani okondwa! Muli odalitsidwa!

________________________________________

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi ndani amene adzakhutitsidwa?

________________________________________

Kodi ndi ndani amene adzaone Mulungu? ____________________

==========================================================================

16. Amene ali ndi njala ya chilungamo adzakhutitsidwa. Oyera mtima adzaona Mulungu.

Kodi ndi ndani amene adzakalandire mphotho yaikulu m'mwamba?

________________________________________

==========================================================================

17. Ndi amene amalondedwa chifukwa cha chilungamo. Ngati inu muli kulondedwa, muli monga m'neneri amene anakhala moyo wokondweretsa Mulungu. Musamayendayenda muli wokwiya ndi kumachita mantha. Muyamikeni Mulungu ndi kumuthokoza chifukwa cha madalitso ake.

Mateyu 5:12:

> Sekerani, sangalalani; chifukwa mphotho yanu ndi yaikulu m'mwamba; pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu.

Mwina inu simungathe kuchita zimenezi mwa inu nokha. Koma Mulungu adzakuthangatani. Adzakuthandizani kuti mulemekeze Mulungu ngakhale pamavuto olimba chotani. Limeneli mwina likhoza kukhala ganizo latsopano kwa inu. Pitani mukauze bwenzi lanu zaphunziro limeneli, kapenanso wina wake wa m'banja lanu. Mukonzekere kudzauza kalasi zimene bwenzi lanu wanena.

==============================================================

18. Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi ndani amene adzakhuta? ______________________________

Kodi ndi ndani amene adzaone Mulungu? ______________________________

______________________________

Kodi ndani amene adzalandire mphotho yaikulu m'mwamba? ______________________________

______________________________

==============================================================

SABATA LACHISANU NDI CHIWIRI: CHIPHUNZITSO CHA KHRISTU CHA PAPHIRI
TSIKU LACHIWIRI: AKHRISTU NDIWO KUWALA NDIPONSO MCHERE WA DZIKO LAPANSI

1. Yesu anali ndi phunziro lalikulu ndi lofunika kwambiri lophunzitsa ophunzira ake. Iye anaŵatengera ku phiri. Iye anaŵaphunzitsa zinthu zina zodabwitsa.

Kuchokera pachiphunzitso cha Yesu cha paphiri, kodi ndi ndani amene ali odalitsidwa chifukwa kuti iwo adzakhutitsidwa?

______________________________

______________________________________________________________

Kodi ndi ndani amene adzadalitsidwa chifukwa adzaona Mulungu?

______________________________________________________________

Kodi ndani amene ali odalitsidwa chifukwa kuti mphotho yawo ndi yaikulu m'mwamba?

______________________________________________

==========================================================================

2. Amene amva njala ya chilungamo ndi odalitsidwa chifukwa iwo adzakhutitsidwa. Oyera mtima ndi odala chifukwa iwo adzaona Mulungu. Amene amalondedwalondedwa chifukwa cha chilungamo ndi odala chifukwa mphotho yawo ndi yaikulu.

Anthu ameneŵa ndi okondwa. Iwo sali monga anthu ena m'dziko lapansi. Iwo amapereka kwa dziko kanthu kena komwe kali kofunika.

(1) Akhristu ndi kuwala ndiponso mchere wa dziko lapansi.
(2) Mateyu 5:16 amati: Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekezeke Atate wanu wa kumwamba.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 5:13 mpaka 20. Kodi Akhristu ndi anthu ofunika m'dziko lapansi?

____________________

==========================================================================

3. Akhristu ndi ofunika kwambiri. Iwo ndi ofunika monga momwe mchere uli wofunikira. Mwina mwake munaiwala kutsira mchere mu chakudya chanu.

Inu muli kukumbukira momwe zinali kukhalira kakomedwe kake. Mwina mwake munali wodabwa kwambiri kuti ndi chifukwa chiyani chakudyacho chinakhala motero kufikira munakumbukira kuti mwaiwala kutsira mchere. Msungwana wina ananena kuti atate ake anakwiya kwambiri chifukwa chakuti anapatsa atatewo chakudya chopanda mchere.

Kodi chakudya chopanda mchere chimakoma motani? ____________________

____________________ ______________________________

================================================================

4. Chimakhala choipa kapena chimakhala chosakoma. Umakhala ndi nthaŵi yovuta kuti uchidye. Chakudya sichimakhala bwino wopanda mchere. Momwemo ndi mmene dziko limakhalira mopanda Akhristu. Akhristu amathandiza dziko kuti likhale malo abwino. Taganizani kuti dziko lidakakhala motani popanda Akhristu.

Kodi Akhristu ndi onga chiyani ku dziko lapansi? ____________________

================================================================

5. Ife tiri monga mchere ku dziko lapansi. Timalipanga kuti likhale bwino. Ife timachita ntchito zabwino. Ife timamvera malamulo. Timakhala okhulupirika. Timakhala okonda ena. Ngati timatsatiradi Khristu moonadi timakhala osiyana ndi anthu ena.

Kodi ndi ayani ali monga mchere ku dziko lapansi? ____________________

================================================================

6. Akhristu ali monga mchere ku dziko lapansi. Taganizirani za moyo wanuwo. Inu munayenera kukhala wosiyana ndi anthu amene ali okuzunguliran i omwe sali Akhristu. Mumayenera kuonetsa mtendere ndi chimwemwe komanso chikondi pamene iwo ali kulongolola.

Mateyu 5:13:

> Koma mcherewo ngati usukuluka, adzaukoleretsa ndi chiyani? Pamenepo sungakwanirenso kanthu konse, koma kuti ukaponyedwe kunja, nupondedwe ndi anthu.

Taganizirani za mchere wa mnyumba mwanu. Ngati suli kukoleramso, kodi mukhoza kuugwiritsa ntchito yanji?

___________________________________

___________________________________________________________________

===================================================================

7. Simungaugwiritsenso ntchito ina iliyonse. Ngati siungakolere sungathandize chakudya. Ndiponso sungagwiritsidwe ntchito pamakungu osupuka ndi opanda ntchito.

Ngati Akhristu ali osasiyana ndi anthu ena, kodi iwo ubwino wawo ndi wotani?

___________________________________________________________

===================================================================

8. Iwo alibe china chabwino mwa iwo. Iwo amangodana ndi wina aliyense. Iwo amataya njira zomwe angathandizire dziko lapansi.

Akhristu ali monga zinthu ziŵiri ku dziko lapansi. Kodi choyamba ndi chiyani?

(1) _________________________ (2) Kuwala

===================================================================

9. Akhristu oonadi ali monga mchere ndipo ali monga kuunika kwa dziko lapansi. Iwo akhoza kupanga malo oipa kuti akhale abwino. Ndipo akhoza kupanga malo a mdima kukhala owala. Kuwala ndi kofunika ku dziko lapansi. Anthu ambiri amaopa mdima. Zinthu zoipa zambiri zimaoneka mu mdima. Nthaŵi zina timakhoza kuona ntchito za mphamvu ya Satana mu mdima. Koma kuunika kumathamangitsa mantha a mu mdima.

Mateyu 5:14:

Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika.

Kodi Akhristu amayenera kukhala owala mumdima uti?

___________________________________________________________________

===================================================================

10. Timayenera kukhala kuunika kwa dziko. Anthu onse otizungulira ife ali kukhala mumdima. Iwo amakhala mumdima wa uchimo. Iwo sadziŵa Mulungu. Iwo sadziŵa mmene angachotsere machimo awo. Iwo sadziŵa komwe mavuto awo amachokera. Komatu njira imeneyo si mmene Akhristufe tiriri. Ngati tiri Akhristu oona sitingathe kukhala obisika. Ife timakhala monga mudzi wa pa phiri. Mwina mwake inu mudaonako mudzi womangidwa pa phiri. Usiku moto umaunikira mowala kwambiri. Kuwalako kukhoza kuonekera mtunda wautali kwambiri.

Kodi ndi m'njira yotani imene muli kuganizira kuti Mkhristu ali monga kuunika?

____________________________________________________

____________________________________________________________

================================================================

11. Mukhoza kuyankha m'njira zambiri. Mukhoza kunena kuti ndi chifukwa chakuti iye amaonekera. Mukhoza kunena kuti chifukwa chakuti ndi wosiyana. Mukhoza kunena kuti ndi chifukwa chakuti njira zake ndi zabwino, kapena kuti iye sakhala ndi moyo wonga wa anthu ena. Akhristu ena amayesa kubisa kuunika kwawo. Iwo amayesa kuchita zinthu monga anthu ena kuti pasakhale wina woŵadziŵa kuti ndi Akhristu. Koma chimenechi sichimene Mulungu amafuna.

Mateyu 5:15:

> Kapena sayatsa nyali ndi kuvundikira m'mbiya, koma aiika iyo pa choikapo; ndipo iunikira onse ali mnyumbamo.

Kodi ndi ndani ali kuunika kwa dziko lapansi? ____________________

================================================================

12. Akhristu ndiye kuunika kwa dziko lapansi. Ngati iwo amayesa kubisa kuunika kwawo iwo si Akhristu abwino. Mulungu amafuna kuti anthu aziona miyoyo ya Akhristu. Kumbukirani kuti akuphunzira anali kuphunzitsidwa phunziro limeneli pa phiri.

Mateyu 5:16:

> Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa kumwamba.

Kodi ndani ananena kuti Akhristu ali kuunika kwa dziko lapansi?

____________________________

13. Yesu ndiye ananena zimenezi. Yesu ananenanso kuti iye mwini ndi kuunika kwa dziko lapansi. Ndi kuchokera kwa Yesu komwe timapeza kuwala kwathu. Ife timamutsata Iye. Ife timachita zimene Iye ananena. Miyoyo yathu ndi yosiyana chifukwa ife tiri monga Iye.

Yohane 8:12:

Pamenepo Yesu analankhulanso nawo, nanena, "Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; Iye wonditsata Ine sadzayenda mumdima; koma adzakhala nako kuunika kwa moyo."

Kodi Akhristu ndi ayani ku dziko lapansi?

(1) ____________________ (2) ____________________

==================================================================

14. Akhristu ndi mchere ndi kuunika kwa dziko lapansi. Ife tiyenera kukumbukira zimenezi nthaŵi zonse. Ngati titaiwala tikhoza kuyesedwa kuti tikhale monga wina aliyense. Tiyeni tiloŵeze ndime iyi.

Mateyu 5:16:

Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa kumwamba.

Ŵerengani ndime imeneyi katatu, yang'anani kumwamba ndi kuyesa kuinena. Ŵerenganinso ndimeyi. Mukanena mosaonera pa buku, ilembeni apa.

Mateyu 5:16: ________________________________________________

________________________________________________________________

________________________________________________________________

==================================================================

15. Yesu anapitiriza kufotokoza za malamulo a Mose. Yesu anati lamulo limeneli linaonetsa mmene anthu akanakhalira moyo wolungama. Iye anati anadzakwaniritsa lamulo lonse la Mose. Chinali chinthu chovuta kwa anthu kukhala osunga malamulo a Mose. Yesu anabwera kudzasintha mitima ya anthu kotero kuti akhoze kukhala moyo wolungama.

Kodi Yesu anati Akhristufe ndife chiyani ku dziko lapansi?

(1) Mchere (2) ____________________

==================================================================

17. Ife ndife mchere ndi kuunika. Timayenera kukhala osiyana. Pamene anthu a m'dziko ationa ife, iwo amayenera kuona kuti sindife ofanana ndi iwo.

Lembani zinthu zina zimene zimakupangani kukhala osiyana ndi dziko lapansi.

________________________________________

Lembani zinthu zina zimene anthu amaziona mziwalo za mumpingo mwanu zomwe ziri zosiyana.

________________________________________

________________________________________

==========================================================

18. Tidzakambirana pa zinthu zimenezi tonse pamodzi.

Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zimene Yesu ananena kuti Akhristufe tiri m'dziko lapansi?

(1) ____________________ (2) ____________________

Lembani Mateyu 5:16: ________________________________________

________________________________________

________________________________________

==========================================================

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: CHIPHUNZITSO CHA YESU CHA PA PHIRI
TSIKU LACHITATU: MUSAKWIYE KAPENA KUCHITA CHIGOLOLO MUMTIMA MWANU

1. Taona kuti Yesu anadzakwaniritsa lamulo la Mose. Iye anakumbutsa ophunzira za zomwe Mose ananena. Tsopano Yesu anaŵauza iwo njira ya kakhalidwe kabwino.

Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zimene Yesu ananena kuti Akhristu tiri m'dziko lapansi monga?

(1) ____________________ (2) ____________________

Lembani Mateyu 5:16: ____________________

____________________

____________________

==========================================================================

2. Yesu anati Akhristu ndi mchere ndi kuunika kwa dziko lapansi. Pezani Mateyu 5:16 m'Buku Lopatulika muone ngati mwalemba bwino. Tsopano siyani Buku Lopatulika lili chitsegulire.

Sichinthu chabwino kukhala monga momwe Afarisi anali kukhalira. Sichinthu chabwino tsopano kukhala m'malamulo a Mose. Yesu anadza kudzasonyeza njira yabwino. Iye anabwera kudzasintha mitima yathu kuti ikhale monga Iye. Yesu analankhula za mkwiyo ndi chigololo.

(1) Ngati mwabwera kudzapembedza Mulungu ndipo mukumbukira kuti muli ndi chifukwa ndi mbale, muyenera poyamba kupita ndi kukayanjana naye.

(2) Ngati muyang'ana pa mkazi ndikumukhumba iye m'njira yolakwa, muli kuchita chigololo mumtima mwanu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 5:21 mpaka 24.

Kodi apa Yesu anali kuphunzitsa za kupha kapena za mkwiyo?

____________________

==========================================================================

3. Iye anali kuphunzitsa za mkwiyo. Lamulo silinalankhule za mkwiyo. Linali kungonena za kupha. Yesu anafuna kuonetsa kuti mkwiyo uli chimodzimodzi kupha mnzako. Ife timadziŵa kuti kukhala wokwiyo sikuthandiza kuthetsa mlanduwo. Izi zimangoonjezera kuti zinthuzo zipitiririrebe kuipa Kukwiira munthu mwa mphamvu ndiko kufunira munthuyo choipa. Pamene ife tilankhula zoipa za munthu wina timadzibweretsera zoipa pa ife tokha.

Mateyu 5:21:

Munamva kuti kunanenedwa kwa iwo akale, "Usaphe, koma yense wakupha adzakhala wopalamula mlandu.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi ndi tchimo liti linaweruzidwa pansi pa lamulo lakale?

________________________________________

=================================================================

4. Kupha kunali kulangidwa ndi chiweruzo. Koma Yesu anali ndi zambiri zonena.

Mateyu 5:22:

Koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wokwiira mbale wake wopanda chifukwa adzakhala wopalamula mlandu; ndipo amene adzanena ndi mbale wake wopanda pake iwe, adzakhala wopalamula mlandu wa akulu; koma amene adzati, "Chitsiru iwe" adzakhala wopalamula gehena wa moto.

Ganizirani ndime imeneyi mosamalitsa bwino. Kodi ndi tchimo liti limene Yesu anati ndi loipa lofanana ndi kupha?

________________________________________

______________________________________________________________

=================================================================

5. Yesu anati kukwiya kuyenera kukhala ndi chilango chimodzimodzi monga kupha. Nthaŵi zina mkwiyo umapha. Umagwira ntchito m'maganizo a munthu Umagwira ntchito m'mitima ya anthu. Ukhoza kuononga miyoyo yawo. Koma ife nthaŵi zina timayesedwa kukhala wokwiya. Kodi ife tikhoza kuchita chiyani ndi mkwiyo? Ife timayenera kupanga mtendere.

Mateyu 5:23-24:

Chifukwa chake ngati ulikupereka mtulo wako pa guwa la nsembe, ndipo pomwepo ukumbukira kuti mbale wako ali ndi kanthu pa iwe, usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nuchoke, muyambe kuyanjana ndi mbale wako, Ndipo pamenepo idza nupereke

mtulo wako.

Kodi ine ndikhoza kupembedza Mulungu ngati pali mkwiyo pakati pa ine ndi munthu wina?

______________________________

===========================================================================

6. Ine sindingathe kupembedza Mulungu ndi mkwiyo uli mumtima mwanga. Mulungu samafuna mapemphero anga kapena mphatso zanga ngati sindiri kubwirizana ndi anthu ena.

Mateyu 5:24:

> Usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nuchoke, nuyambe kuyanjana ndi mbale wako, ndipo pomwepo idza nupereke mtulo wako.

Mwina mwake inu simunaganizire za zimenezi kale lonse. Tsopano taganizirani mosamalitsa bwino. Kodi inu simungathe kuchitira zinthu Mulungu ngati palibe mtendere pakati pa inu ndi mbale?

______________________________

===========================================================================

7. Inu simungathe kupembedza Mulungu. Simungathe kupemphera kwa Iye. Simungathe kupereka mphatso kwa iye. Yesu anati muyenera kuchoka pamalo opembedzawo. Muyenera kupita kwa mbale wanu.

Kodi mumayenera kuchita chiyani ndi mbale wanu musanayambe kuyesa kupembedza?

______________________________

===========================================================================

8. Mumayenera kupanga mtendere ndi Iye. Mumayenera kuyanjana naye. Kukhala oyanjana kumatanthauza kulandirana wina ndi mnzake. Mumakhululukirana eni nokha. Mumachotsa mkwiyo. Koma nanga bwanji ngati munthu winayo safuna kukulandira? Mumayenera kuyesa kuti mumupange amvetsetse. Muyenera kumuonetsa kuti mkwiyo wanu wachoka. Muonetseni kuti mwamukhululukira. Muonetseni kuti mukufuna chikondi pakati pa inu ndi iye. Zimenezi sizinthu zapafupi. Zidzatenga nthaŵi. Zidzatenga nthaŵi ya Mulungu kuti achite mumtima mwanu. Mwina inu simungathe kukhululuka nokha. Pemphani Mulungu kuti aike chikhululukiro mumtima mwanu. Iye adzamva pemphero lanu.

Kodi muyenera poyamba kuchita mtendete ndi ndani musanayambe kupembedza Mulungu?

________________________________________________

===========================================================

9. Mumayenera kuchita zimenezi ndi mbale wanu. Muzichita ndi aliyense amene muli naye chidani. Anthu ambiri amaiwala kuchita zimenezi. Iwo amayesa kupembedza Mulungu koma osaganizira za abale awo. Zoterezi zimafooketsa mpingo. Ndipo zimapangitsa magawano mumpingo. Zimapangitsa kuti anthu adziko azilankhula zoipa za ife.

1 Yohane 4:20:

> Munthu akati, kuti, "ndikonda Mulungu," nadana naye mbale wake, ali wabodza; pakuti iye wosakonda mbale wake amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona.

Ngati mubwera kudzapembedza Mulungu ndipo mukumbukira kuti mbale wanu ali nako kanthu kokangana nanu, kodi muyenera kuchita chiyani?

____________________________________________________________

===========================================================

10. Mumayenera kupita ndi kukapanga mtendere pakati pa iye ndi inu. Chimenechi sichimene anthu adziko amanena. Sichimene lamulo la Mose lidanena. Sichimene Afarisi ananena. Yesu anali kuphunzitsa njira yabwino ya kakhalidwe yoposa lamulo la Mose. Iye anati pakati pa abale sipayenera kuwiirana. Iye anaphunzitsanso kanthu katsopano ka za chigololo.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 5:27 mpaka 32. Werenganinso ndime 28. Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi munthu amachita chigololo motani mumtima mwake?

________________________________

____________________________________________________________

===========================================================

11. Iye amachita zimenezi poyang'ana kwa mkazi namukhumbira. Chimenechi chimatanthauza kumufuna iye m'njira yoipa. Sikugona kokha ndi mkazi komwe kuli kuchita chigololo. Munthu akhoza kuchita chigololo mumtima. Munthu akhoza kubanso mumtima mwake, kapena kuchita bodza mumtima mwake

kapena kupha mumtima mwake. Amenewa ndi machimo ngakhale kuti munthu ali kungowaganizira.

Munthu akhoza kukhala wodzikonda banja lake. M'malo mofuna kufanizira mmene angawasamalire iwo, iye angoganizira ake okha mmene angafune kuwakhutitsira. Iye amaganiza za mmene mkazi wake angamukondweretsere. Iye amaganiza mmene thupi lake lingakhutitsidwire. Iye mayang'ana kwa akazi ena. Iye amaganiza za kuchita chigololo

Kodi ndi ndani adanena kuti ngati utayang'ana pa mkazi ndi kumufuna iye m'njira yoipa, uli kuchita chigololo?

___________________________

====================================================================

12. Yesu ndiye ananena zimenezi. Iye anabwera kudzaphunzitsa njira yakakhalidwe ka moyo, yopambana kwambiri. Iye anabwera kudzapereka moyo watsopano kuti ife tikhoza kukhala m'njira yopambanayi. Iye anaphunzitsa ophunzira mmene angagonjetsere tchimo.

Mateyu 5:29:

> Koma ngati diso lako lamanja likulakwitsa iwe, ulikolowole, nulitaye, pakuti nkwabwino kwa iwe, kuti chimodzi cha ziwalo chiononongeke, losaponyedwa thupi lonse m'gehena.,

Yesu anaphunzitsa kuti ife timayenera kudzithandiza tokha kutembenuka kuchokera ku tchimo. Timayenera kukhala kutali ndi malo amene timayesedwa. Timayenera kuchotsa maso athu ku zinthu zimene zimatiyesa ife. Ndibwino kwa ife kumakana zinthu zina zimene ziri zabwino mwa izo zokha, ngati zitamatiyesa ife. Ife timayenera kukhazika Khristu kuti akhale pakatikati pa miyoyo yathu.

Ngati inu mutayang'ana kwa mkazi ndi kumkhumba m'njira yoipa, kodi Yesu anati muli kuchita chiyani?

___________________________

====================================================================

13. Yesu anati uli kuchita chigololo mumtima mwako. Kumbukirani kuti Yesu anati ubwino wa ntchito zathu umayenera kukhala opitirira za Afarisi. Afarisi anali kufuna kumaoneka abwino. Iwo anali kufuna kuti anthu aziwaganizira kuti ndi abwino. Timayenera kuchita koposa kungooneka kuti ndife abwino. Ife timayenera kukhala abwino m'mitima yathu.

Kodi ndi liti limene munthu amachita chigololo mumtima mwake?

14. Iye amachita zimenezi pamene ayang'ana kwa mkazi ndi kumufuna m'njira yoipa. Mkaziyonso akhoza kuchità chigololo mwa njira yomweyi. Anthu amadziika okha m'mayesero. Iwo amalongolola kunyumba. Mwinanso amakhala kuti sakhala malo amodzi ndi akazi awo. Iwo amangoganiza za iwo eni m'malo mokonda banja. Iwo amafuna kukwaniritsa matupi awo m'malo momanga miyoyo yawo ya uzimu.

Ngati inu mutayang'ana pa mkazi ndi kumufuna iye m'njira yoipa, kodi Yesu ananena kuti muli kuchita chiyani?

15. Yesu anati tiri kuchita chigololo. Chigololo chimatitsogolera m'mavuto ena ambiri. Abambo ndi akazi odzikonda amatopa kukhalira pamodzi. Iwo amatopa kukhalira pamodzi chifukwa chakuti amaganiza za kusiyana ukwati.

Mateyu 5:32:

> Koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuchotsa mkazi wake, kosati chifukwa cha chigololo; am'chititsa chigololo: ndipo amene adzakwata wochotsedwayo achita chigololo.

Yesu anaphunzitsa zinthu zozama zambiri za moyo wa Chikhristu. Ngati inu mubwera kudzapembedza Mulungu ndipo mukumbukira kuti mbale wanu ali nako kachifukwa ndi inu, kodi mumayenera kuchita chiyani?

16. Timayenera kupita ndi kukapanga mtendere ndi iye. Inunso mumayenera kukhala ndi mtendere ndi akazi anu. Kukhala Mkhristu sikungopita ku tchalitchi kokha. Sikungosunga malamulo kokha. Kukhala Mkhristu ndiko kukhala wolungama mumtima mwako. Kumatanthauza kuganizira molondola ndi kukhala ndi moyo wachilungamo.

Mwina mwake mwaphunzira kanthu kena katsopano mphunziro limeneli komwe muli kukaganizira kuti ndi kofunika.

______________________________________________________________________

======================================================================

17. Khalani okonzekera kudzauza anzanu kukalasi zimene mwalemba. Ngati mwabwera kudzapembedza Mulungu ndipo mwakumbukira kuti mbale wanu ali ndi kanthu kena kotsutsana nanu, kodi mumayenera kuchita chiyani?

______________________________________________________________________

Ngati inu muyang'ana kwa mkazi ndi kumufuna iye m'njira yoipa, kodi Yesu anati muli kuchita chiyani?

______________________________

======================================================================